Pofotokoza ubwino umenewu {Ndatumidwa (monga Ntumiki) kwa zolengedwa zonse}, Mufti Ahmad Yaar Khan Na'eemi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wanena kuti: Uneneri ndi malamulo a Mtumiki (SAW) amagwira ntchito pa zolengedwa zonse, zikhala zamoyo kapena zopanda moyo, zanzeru kapena zanzeru. wamisala.

Pofotokoza ubwino umenewu (tcheni cha uneneri chinathera pa ine), Mufti Ahmad Yaar Khan Na'eemi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه walemba: "Ine ndine Nneneri womaliza, amene tcheni cha uneneri chinathera pa ine; palibe nneneri wina m'nthawi yanga, kapena pambuyo

panga.[1]

Aneneri anayi, Sayyiduna Khizr, Sayyiduna Ilyas, Sayyiduna Idrees ndi Sayyiduna 'Isa عَلَيْهِمُ السَّلَام, ndi aneneri popanda chikayiko chilichonse, koma pambuyo pa kubadwa kodalitsika kwa Ntumiki Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَالِهٖ وَسَلَّم. sadza lalikira Shariya yawo.

## Ndine Aqib

4. Ndili ndi mayina asanu. Ine ndine Muhammad; Ndine Ahmad; Ine ndine Mahi (wochotsa), chifukwa Mulungu Wamphanvu zonse adzachotsa kusakhulupirira kupyolera mwa ine; Ine ndine Hashir, pakuti, anthu adzandisonkhanitsira pamapazi anga (ndiye kuti, pambuyo panga tsiku lachiweruzo); ndipo ndine Aqib.[2] Oyera Ntima Tabai'i, Imam Zuhri رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Aqib ndi yemwe pambuyo pake palibe Nneneri wina.[3]

## Tsogoleli wa Atumiki onse

5. Ine ndine Mtsogoleri wa Aneneri, ndipo sindikunena modzikuza; Ine ndine Wotsiriza pakati pa aneneri onse, ndipo ine sindikunena izo ndi kunyada; ndipo ndine woyamba kupembedzera, ndipo ndalandiridwa monga

[1] *Mir'aat, vol. 8, pp. 10-11*

[2] *Bukhari, vol. 2, p. 484, Hadith 3532*

[3] *Muslim, p. 985, Hadith 6107*



www.dawateislami.net

nkhalapakati woyamba, ndipo sindikunena monyadira.[1]

## Kufotokozera za Hadithiyi

Pofotokoza gawo ili (ine ndine Mtsogoleri wa Aneneri) wa Hadith, zalembedwa mu 'Mirat' kuti: Ntumiki woyela صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adzalowa ku Paradiso Aneneri onse asanalowe, ndipo aneneri onse adzatsatira. iye. Momwemo Ntumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi Mtsogoleri wa aneneri.[2]

## خَاتَمُ النَّبِيّٖن

6. Ndithu, ine ndinalembedwa kuti Khaatam-un-Nabiyyeen pamodzi ndi Mulungu Wamphanvu zonse pomwe Sayyiduna Adam عَلَيْهِ السَّلَام anali wowombedwa m'dongo lake.[3]

7. Ndithudi, ine ndine Womaliza mwa aneneri onse, ndipo Nsikiti wanga ndi womaliza pa Misikiti yonse. *(Muslim, p. 553, Hadith 3376)*

## Tanthauzo la Aakhir-ul-Masajid

8. Nkhani ina ili ndi mawu awa: "Ine ndine Womaliza mwa Aneneri onse, ndipo Nsikiti wanga ndi womaliza pa Misikiti

[1] *Daarimi, vol. 1, p. 40, Hadith 49*

[2] *Mirat, vol. 8, p. 28*

[3] *Al-Ihsan bi Tarteeb Sahih Ibn-e-Habban, vol. 8, p. 106, Hadith 6370*



www.dawateislami.net

ya aneneri onse.'[1] (Kutanthauza kuti palibe Nneneri wina aliyense amene adzabadwa pambuyo pa Hazrat Muhammad Arabi صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم,) ngakhale kumangidwa Nsikiti wa Nneneri aliyense.

## Lowani ku Paradiso

9. E inu anthu! Popanda chikayiko, palibe Nneneri aliyense pambuyo panga, ndipo palibe Ummah pambuyo panu. Chenjerani! Ngati inu anthu mumpembedza Mbuye wanu, kupembeza Swala zisanu, kusala m'mwezi wa Ramadhani, ndikupereka Zakaat ya chuma chanu mosangalala, ndi kunvera atsogoleri anu, ndiye kuti mudzalowa ku Paradiso ya Mbuye wanu.[2]

## Mtheradi palibe Nneneri wina pambuyo panga

10. Aneneri عَلَيْهِمُ السَّلَام anali kulamulira Bani Israil. Nthawi zonse Nneneri akamwalira, Nneneri wina ankalowa m'malo mwake. (Koma kumbukirani!) mtheradi Palibe nneneri pambuyo panga. Komabe, posachedwa padzakhala ma khalifa ndipo adzakhala ambiri.[3]

---

[1] *Al-Firdaus, vol. 1, p. 45, Hadith 112*

[2] *Mu'jam Kabeer, vol. 8, p. 115, Hadith 7535*

[3] *Bukhari, vol. 2, p. 461, Hadith 3455*



www.dawateislami.net

## Kufotokozera za Hadith

M'nthawi yanga, palibe Nneneri aliyense amene adzakhala khalifa wanga pamaso panga monga pamene Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام anapita kukabweretsa Tawrah pa Toor, Sayyiduna Haroon عَلَيْهِ السَّلَام anali mulowa mmalo kwa matsiku munthawi ya Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام ndipo palibe nneneri aliyense amene angakhale khalifa wanga mpaka kalekale. Choncho, ma Khalifa anga ndi mafumu amchipembezo changa, makhalifa amu uzimu ndi ma Auliya komanso ndi akatswiri ophunzira. [1]

11. Palibe chimene chinatsalira mu Uneneri, koma kukhala nkhani yabwino. Omutsatira modzichepetsa anafunsa kuti: 'Kodi nkhani yabwino ndi yotani?' Zinalankhulidwa, 'Maloto abwino.' [2]

12. Palibe chimene chidzatsale mu Uneneri pambuyo panga koma nkhani yabwino. Ndiko kuti, maloto abwino omwe munthu mwiniyo ali nawo kapena wina amapangidwa kuti akhale nawo kwa iye. [3]

13. Ndithu, Utumiki ndi Uneneri zidatha, choncho palibe Ntumiki ngakhale Nneneri pambuyo panga. [4]

---

[1] *Mirat, vol. 5, p. 346*

[2] *Bukhari, vol. 4, p. 404, Hadith 6990*

[3] *Musnad Imam Ahmad Bin Hanbal, vol. 9, p. 450, Hadith 25031*

[4] *Tirmizi, vol. 4, p. 121, Hadith 2279*



www.dawateislami.net

14. Ine ndine Muhammad; Ndine Ahmad; Ine ndine Nneneri wachifundo; Ine ndine Nneneri wa kulapa; Ine ndine Nneneri Wotsiriza; Ndine Hashir; Ine ndine Nneneri wankhondo mu njira ya Allah.[1]

15. Ine ndine Ahmad; Ndine Muhammad ndi Muqaffa.[2] Tanthauzo la Muqaffa ndi Aakhir-ul-Anbiya kutanthauza kuti, Omaliza mwa aneneri onse.

16. Ife ndife otsiriza m'nyengo ino, Ndife oyamba pa tsiku lachiweruzo.[3]

## Ummah woyamba kulowa ku Paradiso

Pofotokozera Hadith imeneyi, Wotanthawuzira wa Muslim, Sayyiduna Imam Nawavi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه walemba kuti: "Tanthawuzo la Hadith imeneyi ndikoti ife ndife omalizira pa kubwera pa dziko lapansi, ndipo ndife oyamba pakupambana komanso kulowa ku Paradiso. Choncho, Ummah uwu udzalowa ku Paradiso ma Ummah onse am'mbuyo asanalowe.[4]

[1] *Shamail-e-Tirmizi, p. 215, Hadith 361; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 657*

[2] *Mu'jam Awsat, vol. 1, p. 622, Hadith 2280*

[3] *Bukhari, vol. 1, p. 303, Hadith 876*

[4] *Sharh-e-Muslim-lil-Nawavi, vol. 6, p. 142*

17. Ndithu, tidzakhala omaliza pa onse Padziko lapansi, ndi oyamba Patsiku lachiweruzo, Omwe chiweruziro chidzayambika pa iwo.[1]

## Nkhani ya chidule yathandiza

18. Allah Wamphanvu zonse anandisankhira Ikhtisar, choncho ife ndife omaliza, ndipo tsiku lachiwerudzo ndife oyamba. Limodzi mwa matanthawuzo a gawo (anasankha Ikhtisar) la Hadith lili motere: Ndinadalitsidwa ndi kulondola komwe kumatanthawuza mawu ochepa komanso matanthawuzo ambiri.[2]

19. Ndithu, ine ndinatumizidwa monga Yemwe ndikutsegula mtsinje wa Chifundo ndi kumalizitsa Utumiki ndi Uneneri.[3]

20. Ndinalengedwa koyamba mwa aneneri onse, ndipo ndinatumizidwa pomalizira pa onse.[4]

21. Ine ndine Nneneri womaliza ndipo inu ndinu Umma womaliza.[5]

---

[1] *Muslim, p. 332, Hadith 1982*

[2] *Fatawa Razawiyyah, vol. 30, p. 210*

[3] *Shu'ab-ul-Iman, vol. 4, p. 308, Hadith 5202; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 661*

[4] *Musnad Al-Shamiyeen, vol. 4, p. 34, Hadith 2662*

[5] *Ibn-e-Majah, vol. 4, p. 404, Hadith 4077*

## Chifukwa chokhalira Nneneri wankulu kuposa aneneri onse (Fanizo)

Sayyiduna Sahl bin Salih Hamdani رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anamufunsa Sayyiduna Imam Baqir رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه : Ngati Ntumiki woyela anatumizidwa pambuyo pa aneneri onse عَلَيْهِمُ السَّلَام, anakhala bwanji wolemekezeka Ntumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuposa aneneri onse عَلَيْهِمُ السَّلَام? Iye anati: "Pa tsiku la Misaaq (lonjezo) pamene Allah Wamphanvu zonse anabweretsa ana kuchokera kumisana ya anthu achimuna, Anawapanga kukhala mboni, nati": Kodi ine sindine Mbuye wanu? Kenako oyambirira Mwa onse, Nneneri Woyla anati, eya ndichoncho ndinthu khalabe bwanji. 'Ndichifukwa chake mneneriyu صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Ndipotu iye anatumizidwa komaliza pa anthu onse padziko lapansi.[1]

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

22. Adam عَلَيْهِ السَّلَام ndiye woyamba mwa aneneri onse, Ndipo Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi Womaliza mwa aneneri onse.[2]

23. 'لَوْ كَانَ بَعْدِىْ نَبِيٌّ لَكَانَ عُمَرَبْنَ الْخَطَّابِ' Ndiko kuti, pakadakhala Mneneri pambuyo panga, ndiye Umar. [3]

---

[1] *Khasais-e-Kubra, vol. 1, p. 7*

[2] *Al-Awail-lil-Tabrani, p. 39, Hadith 13*

[3] *Tirmizi, vol. 5, p. 385, Hadith 3706*



www.dawateislami.net

## Kufotokozera za Hadith

Pofotokoza Hadith imeneyi, Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wanena kuti: Ndiko kunena kuti chikhalidwe chake chidali chokwanira kotero kuti khomo la Uneneri likadapanda kutsekedwa, akanatha kukhala Ntumiki kokha ndi chisomo cha Allah wamphanvu zonse. pakuti palibe amene akuyenera kulandira Uneneri chifukwa cha umunthu wake.[1]

24. Abu Bakr ndi wabwino kuposa anthu onse kupatula aneneri[2]

## Pazakhala Aneneri aboza okwana 30

25. Posachedwapa kudzakhala ma Kazzab 30 (anthu abodza aakulu) mu Umma wanga. Aliyense wa iwo adzaganiza kuti iye ndi Nneneri. Koma ine ndine Khaatam-un-Nabiyyeen (n'neneri womaliza), ndipo palibe Nneneri aliyense pambuyo panga.[3]

## Kufotokozera Hadith

Pofotokoza Hadith imeneyi, Mufti Ahmad Yaar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wanena kuti: Aneneri abodza makumi atatu awa ndi omwe anthu anawakhulupirira kuti anali aneneri, ndipo kuwonongeka kwawo

[1] *Fatawa Razawiyyah, vol. 29, p. 373*

[2] *Al-Kamil li Ibn-e-'Adi, vol. 6, p. 484*

[3] *Abu Dawood, vol. 4, p. 132, Hadith 4252*



www.dawateislami.net

kunafalikira. Ntundu wina wa odzinenera uneneri amene anthu sanawakhulupirire analankhula zinyalala ndipo anafa. Iwo ndi ambiri.

Mufti Ahmad Yaar Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wanenanso kuti: "Tinadziwa kuti Khaatam-un-Nabiyyeen amatanthawuza Nneneri womaliza, chifukwa palibe nneneri m'nthawi yake ndi pambuyo pake. Ummah uli ndi mgwirizano pa tanthawuzo limeneli. Amene akunena kuti tanthawuzo lake si 'nneneri womalizira', koma kunena zoona, ndi 'mneneri weniweni', ndi wosakhulupirira.[1]

26. Mu Umma wanga muli Kazzab ndi Dajjal (wabodza ndi wachinyengo kwambiri) (ndipo) anayi ayiwo adzakhala Akazi, ndipo ine ndine Nneneri Womaliza, palibe Nneneri pambuyo panga.[2]

## Kupambana kwa Maula Ali

27. Pamene amapita kunkhondo ya Tabuk, Ntumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anamusiya Hazrat Ali رَضِىَ اللّٰهُ عَنْهُ kumadina! E Ntumiki wa Allah Mukundisiya pakati pa akazi ndi ana." صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Kodi inu simukuvomereza pa izi kuti inu mukhale khalifa wanga monga Musa anamusiya Khalifa wake Haroon pamene anapita kukalankhula ndi Allah Wamphanvu zonse.

---

[1] *Mirat, vol. 7, pp. 219-220*

[2] *Mu'jam Kabeer, vol. 3, p. 169, Hadith 3026*



www.dawateislami.net

Komabe pali kusiyana kuti Haroon عَلَيْهِ السَّلَام anali Nneneri. Chiyambireni Uneneri wanga palibe uneneri kwa aliyense.[1]

## Kufotokozera Hadith

Wotanthawuzira Bukhari, Mufti Sharif-ul-Haq Amjadi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena kuti: Pamene Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام napita kuphiri anampanga Sayyiduna Haroona kukhala khalifa wake kwa kanthawi mpaka kubwerera kwake. Zimenezi zinatha atabwerako. Chitsanzo ichi chinavumbulutsidwa Ntumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anampanga kwa kanthawi Sayyiduna Ali رَضِیَ اللهُ عَنْهُ kukhala Khalifa wake mpaka kubwerera kwake kuchokera ku Tabuk. Ntchito imeneyo inali yongoyang'anira zinthu.[2]

28. Ali akuchokera kwa ine monga momwe Haarun anachokera kwa Musa (poti iye ndi M'bale komanso Khalifa), koma 'لَا نَبِیَّ بَعْدِی' palibe Nneneri aliyense pambuyo panga.[3]

29. Ine ndine Muhammad, Ummi Nneneri (ndi Ntumiki yemwe sanaphunzire kwa aliyense pa dziko lapansi) (ananena katatu), ndipo 'لَا نَبِیَّ بَعْدِی' palibe nneneri aliyense pambuyo panga.

30. Mulungu Wamphanvu zonse anandipatsa chilichonse chimene ndinafuna, koma ndinawuzidwa kuti: Palibe

[1] *Muslim, p. 1006, Hadith 6218; Tirmizi, vol. 5, p. 407, Hadith 3745*

[2] *Nuzha-tul-Qaari, vol. 4, p. 602*

[3] *Tareekh-e-Baghdad, vol. 7, p. 463*

Nneneri pambuyo panga.[1]

## Wanena zowona

31. Angelo adzamufunsa wakufa ali m'manda: 'Kodi Mbuye wako ndi ndani?' 'Kodi chipembedzo chako nchiyani?' 'Kodi Nneneri wako ndani?' Adzati: "Mbuye wanga ndi Mulungu, Yemwe alibe wothandizana Naye; Ndipo Chipembezo changa ndi Chisilamu; Ndipo Nneneri wanga ndi Muhammad (صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم); ndipo iye ndi Nneneri Womaliza. Angelo azati, 'Wanena zowona.'[2]

## Interpretation of a dream

32. Kutanthawuzira maloto a Sayyiduna ibn Ziml رَضِىَ اللهُ عَنْهُ, Wokondedwa Rasool صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Zokhuza ngamila yayikazi wa yiwona kumaloto ako imene ndayikwera, zikusonyeza tsiku lachiweruzo; sipadzkhala Nneneri wina aliyense pambuyo panga, kapena ngakhale sipadzakhala Ummah uliwonse pambuyo pa Ummah wanga.'[3]

## Nur (Kuwala) idzawala patsogolo pawo

33. Ndinthu mopanda chikayiko, tsiku lachimaliziro, Mulungu

---

[1] *Al-Sunnah li Ibn-e-Abi 'Asim, p. 303, Hadith 1348*

[2] *Zikr Al-Maut ma' Mausu'ah lil Imam Ibn Abi Al-Dunya, vol. 5, p. 474, Hadith 254; Sharh-us-Sudoor (Urdu) p. 130 summarised*

[3] *Dalaail-un-Nubuwwah-lil-Bayhaqi, vol. 7, p. 38*



www.dawateislami.net

Wamphanvu zonse adzayitana Sayyiduna Nooh عَلَيْهِ السَّلَام asanayitane wina aliyense ndipo nati: "Kodi ndiyankho lanji mudzapereka kwa Nuhi?" adzati sanatiyitanire kwa Inu, ndiponso sanafikitse uthenga Wanu, ndiponso sanatipatse malangizo, ndiponso sanafotokoze malamulo aliwonse a chabwino kapena choyipa. Sayyiduna Nooh عَلَيْهِ السَّلَام adzayankhula E Ambuye! Ndinawayitanira ku chilungamo kotero kuti Unafalikira pakati pa amlowam'malo ndi am'mbuyo, wina ndi mnzake mpaka kufika Kumeneko kukafika kwa Ntumiki womaliza (Hazrat) Ahmad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Anayilemba ndikuyiwerenga (imene inatchulidwa m'Qur'an yolembedwa ndi kuwerengedwa), ndipo anayikhulupirira ndi kuyivomereza (ndipo) Allah Wamphanvu zonse adzati: "Itanani Ahmad (صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم) ndi Ummah wa Ahmad.' Kenako Ntumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi Ummah wake adzafika pamaso pa Allah wapamwamba mu njira yakuti Nur (Kuwala) idzawawalira patsogolo pawo. Adzapereka umboni wa Nuhi عَلَيْهِ السَّلَام (ndipo adzakhulupirira).,[1]

## Zolengedwa zonse zidzamuyitana Ntumuki omaliza pa tsiku la Chiweruzo

34. Adzandidzera akale ndi amlowam'malo nadzanena:, 'E Ntumiki! Ndiwe Ntumiki wa Allah Wamphanvu zonse

[1] *Al-Mustadrak, vol. 3, p. 415, Hadith 4066; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 690*



www.dawateislami.net

komanso Khaatam-ul-Anbiya kutanthawuza kuti Ntumiki womaliza, tipembezereni ife.'[1]

يَا شَفِيْعَ الْوَرٰى سَلَامٌ عَلَيْک     يَا نَبِيَّ الْهُدٰى سَلَامٌ عَلَيْک

خَاتَمَ الْاَنْبِيَاء سَلَامٌ عَلَيْک     سَيِّدَ الْاَصْفِيَاء سَلَامٌ عَلَيْک

## Ngati Muhammad sakanakhalapo, Sindikanakulengani inu

35. Pamene (Sayyiduna) Adam عَلَيْهِ السَّلَام analakwa pa Ijtihad, anatukula mutu wake wodalitsika ku Arsh ndipo modzichepetsa anawuza Mulungu Wamphanvu zonse kuti: "O, Allah! Ndikukupemphani chikhululuko Chifukwa cha Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.' Allah Wamphanvu zonse anati: 'E iwe Adam! Munamudziwa bwanji Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم? Sindinamulengebe.' Sayyiduna Adam عَلَيْهِ السَّلَام anati: 'E, Allah! Pamene munandilenga ndi mphanvu Yanu, ndinakweza mutu wanga, ndipo ndinawona 'لَآاِلٰهَ اِلَّا اللّٰهُ مُحَمَّدٌ رَّسُوْلُ اللّٰهِ' litalembedwa pa mwendo wa mpando wachifumu (Arsh) ndipo ndinaganiza kuti munalembapo dzina Lanu ndi dzina la Uyo. Wokondedwa kwa Inu kuposa zolengedwa zonse, ndipo ali ndi ulemerero wawukulu kwa Inu. E Adam Wanena zowona. Ndithu, iye Ngokondedwa

[1] *Bukhari, vol. 3, p. 260, Hadith 4712, summarised*



www.dawateislami.net

kwa Ine kuposa zolengedwa zonse. Pamene munandipempha kudzera mwa Muhammad, ndinakukhululukirani Kulakwa kwanu. 'وَلَوْلَا مُحَمَّدٌ مَا خَلَقْتُكَ' kutanthauza kuti, Pakadapanda Muhammad, sindikanakulengani.[1] Mu Tabarani muli kuwonjezera pa izi: Ndipo iye ndi Nneneri womaliza mwa ana anu, ndipo Ummah wake ndi Umma womaliza mwa ana anu.[2]

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

36. Pamene Sayyiduna Adam عَلَيْهِ السَّلَام anafika ku Hind kuchokera ku Paradiso, anali ndi nkhawa. Jibra'ieli anatsika napanga Azan. Pamene dzina lodalitsika linadza, Hazrat Adam عَلَيْهِ السَّلَام anafunsa kuti, 'Kodi Muhammad ndindani صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم?' Kunanenedwa, 'Nneneri Womaliza mwa ana anu.'[3]

## Kutchulidwa mu Tawrah

37. Pamene Tawrah inavumbulutsidwa kwa (Sayyiduna) Musa عَلَيْهِ السَّلَام, Anayiwerenga. Pamene anapeza za kutchulidwa kwa Ummah uwu, modzichepetsa anati kwa Allah

[1] *Al-Mustadrak, vol. 3, p. 517, Hadith 4286*

[2] *Mu'jam Sagheer Juzz Saani, p. 82; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 633*

[3] *Ibn-e-'Asakir, vol. 7, p. 437; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 640*

Wamphanvu zonse, 'O, Mbuye wanga! Ndikupeza Ummah mmenemo kuti uwu ndi womaliza m'nthawi yake komanso woyamba pakupmbana. Choncho upange kukhala Ummah wanga." Allah Wamphanvu zonse anati: 'Uwu ndi Ummah wa Ahmad صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.'[1]

## Oyamba komanso Omaliza

38. Pamene Mulungu analenga (Sayyiduna) Adam عَلَيْهِ السَّلَام ndipo anasonyezedwa ana ake, Anawawona ali opambana kuposa wina ndi mnzake, ndipo pamene anawona kuwala kwakukulu (Nur) kumapeto kwake, Anati kwa Mulungu modzichepetsa. Wamphanvu zonse, 'O, Allah Wamphamvu zonse! Kodi ndindani?' Anati, 'Ndi mwana wako Ahmad.' Iye ndi woyamba, ndipo ndi Womaliza; Ndipo iye ndi Muwomboli woyamba, ndipo Iye ndi woyamba yemwe chiwombolo Chake chidzavomerezedwa. [2]

## Ntumiki woyamba komanso wotsiriza

39. Sayyiduna Abu Hurayrah رَضِيَ اللهُ عَنْهُ wanena kuti: (Usiku wa Mi'raaj) pamene Ntumiki anakumana ndi Aneneri mu thambo, onse analemekeza Mulungu, Wamphamvu zonse,

---

[1] *Dalail-un-Nubuwwah li Abi Nuai'm, p. 33, Hadith 31; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 633*

[2] *Dalail-un-Nubuwwah-lil-Bayhaqi, vol. 5, p. 483; Kanz-ul-Ummal, vol. 11, p. 197, Hadith 32053; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 634*



www.dawateislami.net

ndipo pamapeto pake, Womaliza Ntumiki wa Allah Muhammad Mustafa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Inu nonse mwantamanda Allah, tsopano ine ndikukutamandani: "Kuyamikidwa konse nkwa Allah wapamwambamwamba Yemwe wanditumiza ine monga chifundo kwa zolengedwa zonse monga wofalitsa nkhani yabwino. ndi Yemwe amachenjeza anthu onse. Mbuye wandivumbulutsira Qur'an yopatulika yomwe ili ndi kufotokoza monveka bwino pa chilichonse. Wa upanga Ummah wanga kukhala wopambana kuposa ma Ummah onse omwe anatulukira pakati pa anthu ndipo waupanga kukhala woyamba ndi womaliza. Wandikwezera kundikumbukira, nayamba ndi ine Uneneri ndikuukwaniritsa pa ine." Pamene Sayyiduna Ibrahim Khalilullah عَلَيْهِ السَّلَام atanva izi anati kwa Aneneri onse: "Chifukwa cha makhalidwe amenewa, Muhammad (صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم) ndi wabwino kuposa inu nonse. Kenako Ntumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapita ku Sidra-tul-Muntaha. Kenako Allah Wamphanvu zonse anamulankhula (Kalam) [monga kuyenerana ndi ulemerero Wake], nati: 'Ndinakulenga iwe Aneneri onse asanaze koma ndinakutumiza pambuyo pa Aneneri onse, ndipo ndidakupangani kukhala Faatih ndi Khaatam (otsegula ndi omaliza).'[1]

[1] *Tafseer Tabri, vol. 8, pp. 9-11, Hadith 22021; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 637*

## 'اَنَا لَهَا' adzakhala mawu a Bwana wanga

40. Anthu akadzakhumudwa ndi chi ombolo chochokera kwa Aneneri onse عَلَيْهِمُ السَّلَام, adzapita kwa Sayyiduna 'Isa Ruhullah عَلَيْهِ السَّلَام kukapempha uwomboli. Adzati: 'Sindingathe kuchita zimenezi koma (Sayyiduna) Muhammad Khaatam-un-Nabiyyeen (womaliza pa Aneneri onse) صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ngothekera ndipo iye ali pano.' Anthu akadzandidzera ndikundipempha chiwombolo, ndidzanena 'اَنَا لَهَا' kutanthawuza kuti ine ndichita (ntchito imeneyi). [1]

*Kahayn gay aur Nabi 'اِذْهَبُوْا اِلٰى غَيْرِى'*

*Mayray Huzoor kay lab per 'اَنَا لَهَا' ho ga*

## Kufotokozera ndakatulo ya Hasan

Tsiku lachimaliziro, pamene anthu adzapempha chiombolo kwa Aneneri, onse adzati: "Pita kwa wina wosakhala ine." Akadzakhumudwa paliponse, adzapita pa matso pa Ntumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi kukapempha unkhala pakati (mapembezero). Choncho صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adzati: '(Ndithudi) Ine ndichita ntchito imeneyi.'

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب     صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

[1] *Musnad Abu Ya'la, vol. 2, p. 368, Hadith 2324; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 639*



www.dawateislami.net

## Sindikubisa chilichonse kupatula... (fanizo)

Oyela Mtima Taba'i, Sayyiduna Ka'b-ul-Ahbaar رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: "Mwa amene anali ndi chidziwitso cha Taurat, bambo anga anali wodziwa kwambiri. Chilichonse chimene Mulungu Wamphanvu zonse anavumbulutsa kwa Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام palibe amene anadziwa kuposa bambo anga. Amandigawira chidziwitso chake. Pamene anatsala pang'ono kumwalira, anandiyitana nati: 'E mwana wanga! Ukudziwa kuti ine sindinakubisireni kudziwa kwanga kwa Torah, koma muli masamba awiri omwe akutchula Ntumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amene nthawi yake yofika yakwana. Sindinakudziwitse zamasamba awiriwa (Kupangira ena anganene kuti ndi Nneneri) ndikumtsata. Pamaso panu pali kagawo kakang'ono komwe ndimasunga masambawo ndikuvindikirapo ndi dothi. Usawawona masamba amenewo panopa. Akadzadza Nneneri (صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم) ndipo Mulungu Wamphanvu zonse akakuchitirani chifundo, mudzamtsate.' Atatha kunena izi, anamwalira. Potha kuyikidwa mmanda, ndinali wofunitsitsa kuwona masamba amenewo. Pomaliza, ndinatsegula niche ndikupeza masamba omwe amawerengedwa:

مُحَمَّدٌ رَّسُوْلُ اللّٰهِ خَاتَمُ النَّبِيّٖنِ لَا نَبِيَّ بَعْدَهٗ مَوْلِدُهٗ بِمَكَّةَ وَ مُهَاجَرُهٗ بِطَيْبَةَ

kutanthawuza kuti, Muhammad ndi Ntumiki wa Allah Wamphanvu zonse, Nneneri womaliza; Palibe Nneneri pambuyo



www.dawateislami.net

pake; kubadwa kwake kudzachitikira ku Makka ndipo adzasamukira ku Madina.[1]

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

# Mawu asanu a maswahaba odalitsika komanso ama Taba'en

## 1. Mawu opatulika pakati pa mapewa onse awiri

Sayyiduna Jabir bin Abdullah رَضِیَ اللهُ عَنْهُ anati: "Pakati pa mapewa awiri a Sayyiduna Jabir bin Abdullah رَضِیَ اللهُ عَنْهُ mawu wotsatirawa analembedwa 'مُحَمَّدٌ رَّسُوْلُ اللّٰهِ خَاتَمُ النَّبِيّٖن صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم', mwachitsanzo, Muhammad (صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم) ndi Ntumiki wa Allah komanso ndi Ntumiki womaliza..'[2]

## 2. Iye akanapanda kulengedwa, palibe chimene chikanalengedwa

Sayyiduna Salman Farsi رَضِیَ اللهُ عَنْهُ wanena kuti Sayyiduna Jibraeel Amin عَلَيْهِ السَّلَام anadza kwa Mtumiki woyela adati, 'E, iwe Nneneri

[1] *Khasaais-e-Kubra, vol. 1, p. 25*

[2] *Tareekh Dimashq, vol. 2, p. 137; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 634*



www.dawateislami.net

wa Allah! Mbuye wako wanena: “Ndithu, Ine ndakusankha iwe kukhala womaliza mwa Aneneri onse, ndipo sindinalenge wina aliyense wolemekezeka kuposa iwe p Maso Panga. Dzina lako ndaliphatikiza ndi Langa kuti kulikonse kumene ndidzakumbukiridwe Iwenso Udzakumbukiridwe. Ndithu, Ine ndalenga dziko ndi amene ali mmenemo kuti ndiwavumbulutsire Ulemu ndi ndinyota zako pamaso panga. Ndikanapanda kukulengani, sindikanalenga thambo, dziko lapansi, ndi zonse zili mmenemo.”[1]

*Hay unheen kay dam qadam ki bagh-e-‘aalam mayn bahar*
*Woh na thay ‘aalam na tha, gar woh na hoon ‘alaam nahin*

## Kufotokozera ndakatulo ya Raza

Kukhala ndi moyo ndi kukongola konse kwapadziko lapansi kumabwera chifukwa cha Ntumiki Womaliza wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Ntumiki wanga wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم akanapanda kubwera pa dziko lapansi, dziko lapansi silikanakhalapo, ngakhalenso dziko lapansi silikanapezeka.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب     صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

[1] *Tareekh Dimashq, vol. 2, pp. 136-137; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 636*



www.dawateislami.net

## 3. Message to Sayyiduna Ibrahim عَلَيْهِ السَّلَام

Sayyiduna Amir Sha'bi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: 'Sahifay[1] (Mawu akumwamba) amene Allah Wamphanvu zonse anawavumbulutsa kwa (Sayyiduna) Ibrahim (Khalilullah عَلَيْهِ السَّلَام) pambuyo pa fuko mwa ana anu mpaka kudzafika Ummi Nneneri (Ntumiki yemwe ali ndi chidziwitso popanda kuphunzira kwa aliyense pa dziko lapansi) Khaatam-ul-Anbiya (صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم) adzabwera.[2]

Mbuye wanga, A'la Hazrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه walemba:

*Aisa Ummi kis liye minnat kash-e-ustad ho*
*Kiya kifayat us ko 'اِقْرَاْ رَبُّكَ الْاَكْرَمُ' nahih*

## Explanation of Raza's poetry

Allah Wamphanvu zonse Iye anamphunzitsa Ntumiki Womaliza, zatchulidwa pa Gawo 30 la Surah 'Alaq. Allah Wamphanvu zonse anamphunzitsa Yekha; chifukwa chani avutike kufunafuna maphunziro kwa mphunzitsi wina aliyense pa dziko la pansi? Pokhala 'Ummi' ndi chozizwitsa chake chantengo wapatali, kuwonetsera kuti sanaphunzire kwa wina aliyense, koma anapeza maphunziro onse a sayansi apa dziko lapansi.

---

[1] *Mu Dikishonare, Pa matsamba amene (liwu) kalam mawu a Allah alembedwa amatchedwa "Sahifa," muteminologe, ndi mawu akumwamba amene atsika kwa Atumiki mmutimabuku (Noor-ul-Irfan.tsamba.977)*

[2] *Al-Tabqaat Al-Kubra li Ibn-e-Sa'd, vol. 1, p. 130; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 635*

## 4. Revelation to Sayyiduna Ash'iya عَلَيْهِ السَّلَام

A Taba'i saint, Sayyiduna Wahb bin Munabbah رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه, has stated that Allah Almighty sent revelation to His beloved Prophet, Sayyiduna Ash'iya عَلَيْهِ السَّلَام, declaring, 'I am going to send an Ummi Prophet, through whom I will "open" deaf ears, heedless hearts, and blind eyes. His birth will take place in Makkah, he will migrate to Madinah, and his kingdom is in 'Syria'. I will surely make his Ummah better and greater than all Ummahs that emerged among people. I will make other books culminate in their book, other Shari'ahs in their Shari'ah, and other religions in their religion.[1]

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kufotokoza za Ufumu wa Syria'

E, inu Onkonda Ntumiki womaliza komanso ma Ahl-e-Bayt! Hadith yomwe yatchulidwa kumeneyi ikuphatikizanso kuti ufumu wa Ntumiki wathu wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم udzakhala ku Syria. Pazimenezi, ndikubweretsereni ngale ya Madani yochokera mu Fatawa Razawiyyah: Bwana wanga, A'la Hazrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wanena kuti, 'Sayyiduna Ameer Mu'awiyah رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ ndi woyamba mu ufumu wa Muhammad . Ndipo zafotokozedwanso mu Taurat yopatulika kuti: 'مُوْلِدُهٗ بِمَكَّةَ وَمُهَاجَرُهٗ طَيْبَةَ وَمُلْكُهٗ بِالشَّامِ' Nneneri Womaliza صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

[1] *Dalaail-un-Nubuwwah li Abi Nuai'm, p. 36, Hadith 33; Al-Khasais-ul-Kubra, vol. 1, p. 23; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 635*

adzabadwira ku Makka, nasamukira ku Madina, ndipo ufumu wake udzakhala ku Syria. Choncho ngakhale Ameer Mu'awiyah رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ aNali ndi ufumuwo koma ndithu, unali ufumu wa Ntumiki Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.'[1]

*Har Sahabi'ay Nabi! ...... Jannati Jannati*
*Sab Sahabiyat bhi! ...... Jannati Jannati*

*Char Yaraan-e-Nabi ...... Jannati Jannati*
*Hazrat-e-Siddeeq bhi...... Jannati Jannati*

*Aur Umar Farooq bhi ...... Jannati Jannati*
*Usman-e-Ghani ...... Jannati Jannati*

*Fatimah aur Ali ...... Jannati Jannati*
*Hayn Hassan Husayn bhi...... Jannati Jannati*

*Walidayn-e-Nabi ...... Jannati Jannati*
*Har zoja'ay Nabi ...... Jannati Jannati*

*Aur Abu Sufyan bhi...... Jannati Jannati*
*Hayn Mu'awiyyah bhi ...... Jannati Jannati*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب     صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

[1] *Fatawa Razawiyyah, vol. 29, p. 357*



www.dawateislami.net

## 5. Chivumbulutso kwa Sayyiduna Yaqoob عَلَيْهِ السَّلَام

Sayyiduna Muhammad bin Ka'b Qurazi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه wanena kuti Allah Wamphanvu zonse anatumiza chivumbulutso kwa Sayyiduna Yaqoob عَلَيْهِ السَّلَام kuchokera kwa ana ako mpaka nditantuma Ntumiki woyela صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amene Ummah wake udzamanga Bayt-ul-Muqaddas mokweza, ndipo iye ndi Ntumiki wotsiriza, dzina lake ndi Ahmad. صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم'.[1]

[1] *Al-Tabqat Al-Kubra li Ibn-e-Sa'd, vol. 1, p. 129; Fatawa Razawiyyah, vol. 15, p. 635*



www.dawateislami.net

# Mawu a Kumaliza kwa Utumiki

| |
|---|
| Muhammad-e-Mustafa<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Ahmed-e-Mujtaba<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Wokondedwa wa Amna<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Mfumu ya maiko onse awiri<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Mtsogoleri wa Aneneri onse<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Wokondedwa wa Allah<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |

| |
|---|
| Wopembezera Wankukulu<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Chiyembekezo cha ochimwa<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Chikhulupiriro cha Fatimah<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Mawu a Aisha<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Chikhulupiriro cha ma Sahaba onse<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Chikhulupiriro cha Banja lodalitsika<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Chikhulupiriro cha Ghaws-e-Pak<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |



www.dawateislami.net

| |
|---|
| Oyela ntima nawonso ananena<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Akuluakulu komanso ana amanena<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Ngakhale mwana aliyense amati<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Chikhulupiriro cha Raza<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |
| Mawu a Attar<br>“Omaliza mwa Aneneri onse” |



www.dawateislami.net

## Perekani kabukuka kwa wina aleyense mukatha

Pezani mphotho pogawira timabuku ta Maktaba-tul-Madīnaĥ ndi timapepala ta Madanī tili ndi ngale za nthawi yaukwati, maliro, Ijtimā'āt, 'Urs, Nkumano wa Mīlād ndi zina zotero. Khalani ndi chizolowezi chosunga timabuku mu shopu yanu kuti mupatse mphatso kwa makasitomala anu ndi cholinga chopeza mphotho. Tumizani kabuku kamodzi ka kolimbikitsa ma Sunnaĥ- kapena kabuku kamene kamakhala ndi ngale za Madanī ku nyumba iliyonse m'dera lanu mothandizidwa ndi ana kapena anyamata amapepala, akumakwera.

Ofunafuna kudandawula (pakusiyana ndi) Madinah, (ku ikidwa ku) Jannat-ul-Baqi', Kukhululukidwa popanda kuweruzidwa machimo komanso (kulowetsedwa ku) Jannat-ul-Firdaus komanso kuyandikana ndi Ntumiki oyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم mu jannahmo.

17 Rabi'-ul-Awwal
1444 AH
**14-10-2022**



www.dawateislami.net

# Bibliography


| Buku | Mulembi | Buku | Mulembi |
|---|---|---|---|
| Quran-e-Majeed | | Zikr Al-Maut | Al-Maktaba Al-‘Asriyyah Beirut |
| Kanz-ul-‘Irfan | Maktaba-tul-Madinah Karachi | Kanz-ul-‘Ummal | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut |
| Tafseer Tabri | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut | Al-Istazkaar | Dar-ul-Ihya Al-Tiras Al-‘Arbi Beirut |
| Taawilaat-e-Ahl-e-Sunnah | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut | Sharh Muslim | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut |
| Tafseer Khazain-ul-‘Irfan | Maktaba-tul-Madinah Karachi | Ashi’a-tul-Lam’aat | Quita |
| Sirat-ul-Jinan | Maktaba-tul-Madinah Karachi | Nuzha-tul-Qaari | Fareed Book Stall Lahore |
| Bukhari | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut | Mir’aat | Ziya Al-Quran Publications Lahore |
| Muslim | Dar-ul-Kitab Al-‘Arbi Beirut | Shamail-e-Tirmizi | Dar-ul-Ihya Al-Tiras Al-‘Arbi Beirut |

| Buku | Mulembi | Buku | Mulembi |
|---|---|---|---|
| Abu Dawood | Dar-ul-Ihya Al-Tiras Al-‘Arbi Beirut | Dalaail-un-Nubuwwah-lil-Bayhaqi | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut |
| Tirmizi | Dar-ul-Fikr Beirut | Dalail-un-Nubuwwah li Abi Nuai’m | Al-Maktaba Al-‘Asriyyah Beirut |
| Ibn-e-Majah | Dar-ul-Ma’rifa Beirut | Khasais-ul-Kubra | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut |
| Daarimi | Dar-ul-Kitab Al-‘Arbi Beirut | Sharh Shifa | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut |
| Musnad Ahmad | Dar-ul-Fikr Beirut | Shan-e-Habib-ur-Rehman | Na’eemi Kutub Khanah Pakistan |
| Mu’jam Kabeer | Dar-ul-Ihya Al-Tiras Al-‘Arbi Beirut | Tabqat Kubra | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut |
| Mu’jam Awsat | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut | Tareekh Baghdad | Dar-ul-Kutub Al-Imiyyah Beirut |
| Mu’jam Sagheer | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut | Ibn-e-‘Asakir | Dar-ul-Fikr Beirut |

| **Buku** | **Mulembi** | **Buku** | **Mulembi** |
|---|---|---|---|
| Musnad Shamiyeen | Mo'assasa-tur-Risalah Beirut | Mukhtasir Tareekh Dimashq | Dar-ul-Fikr Beirut |
| Mustadrak | Dar-ul-Ma'rifa Beirut | Al-Kamil | Dar-ul-Kutub Al-Imiyyah Beirut |
| Musnad Abu Ya'la | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut | Fatawa Aalamgiri | Dar-ul-Fikr Beirut |
| Al-Firdaus bi masoor-il-Khittab | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut | Fatawa Razawiyyah | Raza Foundation Lahore |
| Shu'ab-ul-Iman | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut | Sharh-us-Sudoor (Urdu) | Maktaba-tul-Madinah Karachi |
| Al-Ihsan bi Tarteeb Sahih Ibn-e-Habban | Dar-ul-Kutab Al-Imiyyah Beirut | Muntakhib Hadeesayn | Maktaba-tul-Madinah Karachi |
| Al-Sunnah | Daar Ibn-e-Hazam Beirut | Hadaiq-e-Bakhshish | Maktaba-tul-Madinah Karachi |
| Al-Awail | Dar-ul-Furqan Beirut | Al-Malfooz | Maktaba-tul-Madinah Karachi |

# Burden of (keeping an unowned) date

Some people were sitting in Bayt-ul-Maqdas after offering Nafl Salah. A pious man said: Ibrahim Bin Adham has been deprived of the pleasure of worship for 40 days. Hearing this, he رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه said: Hadrat! You are telling the truth, but for what reason was I deprived of it? The pious man said: You had bought dates on a such-and-such day in Basra. A date belonging to the seller was lying there. You picked it up thinking it was yours (that date is the reason for your deprivation of the pleasure of worship). Hadrat Ibrahim Bin Adham رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه travelled to Basra to have that date forgiven and got it forgiven. *(Tazkra-tul-Awliya`, vol. 1, p. 102, summarised)*

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagaran
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan
UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 7213
Web: www.maktabatulmadinah.com | E-mail: feedback@maktabatulmadinah.com